# STVP ilimbikitsa ulimi wa njuchi ku Nsanje

Wolemba
MARTIN GELA JNR

Anthu a m'dera la T/A Tengani m'boma la Nsanje koma ayandikira nkhalango ya Matandwe ayamikira ntchto yomwe Shire Valley Transformation Programme (SVTP) yakhazikitsa yolimbikitsa ulimi wanjuchi m'deralo.

Poyankhulapo pambuyo powaphunzitsa maphunziro akawatedwe ka njuchi ndi kasamalidwe kabwino ka uchi wokololedwawo, wapampando wa Mnthumba Beekeeping Club, a Emmanuel Banda wati tsopano atseguka maso za momwe angachitire ulimiwu.

"Taphunzira momwe tingasungire bwino njuchi komanso momwe tingachitire kuti akhale ndi uchi wopereka chikoka kwa ogula kuchokera kwa a mkhala kale pantchitoyi pofuna kusiya kuononga nkhalango podula mitengo ndi kuotcha makala," adatero iwo.

A Banda adati akufuna kukhala m'gulu la Amalawi omwe akuchita zaphindu ndi ulimiwu popeza azipakira m'mabotolo ndi kumagulitsa misika ikuluikulu komanso kunja kwa dziko lino.

Pogwirizana ndi a Banda, a James Piriminta adati chidwi chawo chachoka pootcha makala kudula mitengo yocheka matabwa ndi kuika chidwi chawo poika ming'oma m'nkhalango ya Matandwe kwinaku abzala mitengo mphepete mwa mitsinje ya Namiyala, Nyamithuthu, Ndiola ndi ina.

Mkulu woona za nkhalango m'boma la Nsanje a Noel Moyo ati ulimiwu uthandizira kuti mchitidwe woononga nkhalango ndi ntchito zina ngati kutentha makala ndi kucheka matabwa kuchepa m'bomalo.

Iwo adati: "Izi zipangitsa kuti anthuwa azipindula ndi nkhalango popeza nkhalangozi zikhala zikuwapindulira alimiwa popanda kudula mitengo kapena kuononga pokhala pa nyama za m'nkhalangomu."

Adaonjeza kuti anthu osauka omwe amasowa mpamba woyambira mabizinesi apindula popeza safuna mpamba komanso zinthu zina zoonjezera ngsti mbewu ndi fetereza akanalima zomwe zimafunika kuti mlimi akolole zochuluka.



Banda m'tisheti yachikasu ndi anzake akuika ming'oma

Mkulu woyendetsa zilinganizo ngati izi Dr Gibson Mphepo adati ulimi wa njuchi ndi wokhazikika ukagwiridwa bwino ndi kusamalira ndipo ungapindulire miyoyo ya anthu a kumudzi komanso kupindula pathanzi ndi madyedwe abwino komanso amathandizira kuchiza matenda a pakhungu, zilonda zosapola ndi mabala omwe amabwera munthu akapsa.

Mkulu wa zankhalango m'dziko lino a Titus Zulu omwenso akuyang'anira ntchitoyi alimbikitsa alimiwa kuti azisamalira njuchizo ponena kuti ndi gwero la zachuma, chakudya, mankhwala komanso ndi mbali yimodzi yachiledwe.

A Zulu adati ayesetsa kuti nkhalango zikusamalidwa pambali yoti zikupindulira anthu omwe azizungulira.

Bungwe la SVTP likugwira ntchitoyi ndi thandizo la ndalama kuchokera kubanki ya padziko lonse (World Bank). ■




Kodi mukudziwa kuti moto wolusa umaononga chakudya cha nthaka ndipo zotsatira zake sikhala ndi chakudya chodyetsera mbewu? Nanga mukudziwa kuti kulekelera ziweto ndikumangoziyendera m'minda kumasokoneza kasanjidwe ka nthaka m'mundamo?Alimi apewe moto olutsa pokonza zotchingira pachizungu amati *fire break* kuti ngati m'munda mwina mwabuka moto usafalikire m'munda mwawo. Uthenga woteteza minda ku moto komanso ziweto ukuyenera kufalikira ponseponse pofotokoza za kuipa koyatsa moto m'minda ya mbewu komanso kulekelera ziweto kuti zizingodziyendera. Akatero apindula nayo ■